


Mpingo Wonyengedwa Ndi Dziko

 Yesu Khristu, Mwana Wake, ndipo watipatsa ife zinthu zonse mwaulere mwa Khristu. Ife ndife oyamikira kwa Inu, Ambuye, chifukwa cha mwayi umene ife tapatsidwa mwa Nsembe yaikulu yapamwamba iyi yomwe Yesu anatiperekera ife pa Kalvare, yomwe inatinyanjani ife kubwerera mu chiyanjano ndi kukondedwa ndi Inu, kuti ife tikhoze kukhala nacho chitonthozi ichi cha kudziwa kuti kwalembedwa “Ngati inu mukhala mwa Ine, ndi Mawu Anga mwa inu, inu mukhoza kupempha chimene inu mungafune, ndipo icho chidzachitidwa kwa inu.” Tsopano, ife tiri oyamikira chifukwa cha ichi, ndipo tikupemphera kuti Inu mutipatse ife chikhulupiriro kuti tikhulupirire izo ndi zonse zimene ziri mkati mwathu.

² Tsopano tiloreni ife tiyike pambali, Ambuye, chothodwetsa chirichonse cha tsiku, chosamalira chirichonse cha moyo uno, njira yonse kuchokera kwa osamalira pano mpaka kwa m’busa, kuti pasakhale pali chinthu china mu malingaliro athu tsopano, koma tikhale tikuyembekezera, kumvetsera molemekeza kuti Mzimu Woyera uyankhule kwa ife, kuti ife tikhoze kukwaniritsa chinachake chabwino, kuti tidziwe zochuluka za Inu, mwa kusonkhana kwathu palimodzi. Pakuti, Ambuye, moona ndicho chifukwa chomwe ife tadzera pa tsiku lotentha ili. Yankhulani kwa ife kupyolera mu Mawu Anu amoyo, ndipo mulole Mawu amoyo akhale mwa ife ndi kukhazikika mwa ife, kuti ife tikakhoze kuwumbidwa ndi kupangidwa, osati kwa dziko, koma kukhala osinithidwa mwa kukonzanso kwa mzimu wathu, kupita mu mawonekedwe a Mwana wa Mulungu. O, mitima yathu imanjenjemera pamene ife tiganiza, ndipo chimwemwe chimasefukira pa miyoyo yathu, kudziwa kuti ife tikhoza kutchedwa ana amuna ndi aakazi a Mulungu. Ife tikuyima pa mphepete pomwe pa Kudza Kwake kwachiwiri, ndipo mafuko onse ndi maufumu akunjenjemera pansu pa mapazi athu, zinthu zonse za mdziko zikutha, koma podziwa kuti tsiku lina Iye adzadza ndipo adzatitengera ife kupita ku Ufumu kumene sikudzakhala konse mapeto, kapena, iwo siudzasunthidwa konse. Ndipo kuganiza kuti ife tiri tsopano o—omvera a Ufumu umenewo! O Mulungu, dulani mtima wathu ndi makutu lero, mwa—mwa Mzimu Woyera, kupyolera mu kutsuka kwa madzi a Mawu. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina Lake ndi kwa ulemerero Wake. Amen.

³ Ine ndikukhumba kuti ndiyandikire phunziro mmawa uno. Pakuti, ine ndimati ndiyankhule pa chinachake chosiyana pang’ono ngati pakanati pakhale msonkhano wamachiritso, koma ife tinalengeza kuti makadi a pemphero aperekedwe pa eyiti, mpaka hafu pasiti eyiti kapena naini koloko. Ndipo ine

basi. . . Billy anabwera ku nyumba maminiti pang'ono apitawo ndipo iye anati uko kunalibe nkomwe aliyense kuno, kotero iye sanapereke makadi a pemphero. Kotero ife tidza. . . Ine ndinaganiza za kutenga nkhani iyi, ya kuwukonza mpingo. Ndipo ine ndikufuna kuti ndiyankhule pa phunziro la: *Mpingo Wonyengedwa, Ndi Dziko*. Ine ndikukhumba kuti ndiwerenge zina tsopano kuchokera mu Bukhu la Oweruza, mutu wa 16, kuyambira ndi ndime ya 10.

Ndipo Delila anati kwa Samsoni, Taona, iwe wanditonza ine, ndipo wandiuza ine zabodza; tsopano undiuze ine, ine ndikukupempha iwe, momwe iwe ungati umangidwire.

Ndipo iye anati kwa iye, Ngati iwe undimanga ine zolimba ndi zingwe zatsopano, zomwe sizinagwirepo ntchito, ndiye ine ndidzakhala wofooka, ndi kukhala monga munthu wina.

Delila chotero anatenga zingwe zatsopano ndipo anamumanga nazo iye, ndipo anati kwa iye, Afilisti ali pa iwe, Samsoni. Ndipo apo panali obisala molindira ali m'chipinda. Ndipo iye anazidula izo kuchokera pa mikono yake monga ngati ulusi.

Ndipo Delila anati kwa Samsoni, Mpaka tsopano iwe wandipusitsa ine, ndipo wandiuza ine mabodza: undiuze ine momwe iwe ungamangidwire. Ndipo iye ananena kwa iye, Ngati iwe uluka. . . mangongo asanu ndi awiri a pamutu panga ndi ukonde.

Ndipo iye analimangirira ilo ku chokanikiza, ndipo anati kwa iye, Afilisti ali pa iwe, Samsoni. Ndipo iye anagalamuka ku tulo take, ndipo anachokapo ndi chokanikizira pa chithabwa, ndi ukonde womwe.

Ndipo iye anati kwa iye, Unganene iwe bwanji, ine ndikukukonda iwe, pamene mu mtima wako suli ndi ine? iwe wanditonza ine nthawi zitatu izi, ndipo. . . wandiuza ine momwe mwagona mphamvu yako yaikulu; ndipo sunandiuze ine momwe mwagona mphamvu yako yaikulu.

Ndipo kunali kuti, pamene iye anali atamuumiriza iye tsiku ndi tsiku ndi mau ake, ndipo namkakamiza iye, mwakuti moyo wake unavutika pafupi kufa.

Ndipo iye anamuuza iye mtima wake wonse, nanena kwa iye, Sipanapite lumo pa mutu panga; pakuti ine ndakhala ndiri Mnaziri kwa Mulungu, kuchokera mu chiberekero cha amai anga: ngati ine ndimetedwa, ndiye mphamvu zanga zindichokera ine, ndipo ndidzakhala wofoka, ndi kukhala monga munthu wina aliyense.

Ndipo pamene Delila anaona kuti adamfotokozero mtima wake wonse, iye anatumiza ndipo anayitana . . . akalonga a Afilisti, kuti, Bwerani kano kokha, pakuti iye wandisonyeza ine mtima wake wonse. Ndipo akalonga a Afilisti anadza kwa iye, ndipo anafunafuna ndalama, kapena anabweretsa ndalama mu dzanja lake

Ndipo iye anamupangitsa iye kugona pa maondo ake; ndipo anaitanitsa mwamuna, ndipo iye anamuza iye kuti amete mangongo ake asanu ndi awiri pa mutu wake; ndipo . . . anayamba kumuzunza iye, ndipo mphamvu zake zinamuchokera iye.

Ndipo iye anati, Afilisti ali pa iwe, Samsoni. Ndipo iye anagalamuka m'tulo take, ndipo anati, ine ndituluka monga pa nthawi zina poyamba, ndi kudzitakasuka ndekha. Ndipo sanadziwe kuti YEHOVA anali atachoka kwa iye.

4 Tsopano ine ndikukhumba kuti ndiwerenge, kwa mutu wa phunziro ili, wopezeka mu Bukhu la Chivumbulutso, mutu wa 2, kuyambira ndi ndime za 21 ndi 23.

Ndipo Ine ndinampatsa iye danga kuti alape za ziwerewere zake; ndipo iye sanalape ayi.

Taonani, Ine ndidzamuponya iye mu kama, ndi iwo amene achita chigololo ndi iye kupita mu chisautso chachikulu, kupatula iwo atalapa za zochita zawo.

Ndipo Ine ndidzapha ana ake ndi imfa; ndipo mipingo yonse idzadziwa kuti Ine ndine iye yemwe afufuza impso ndi mitima: ndipo ine ndidzapereka kwa aliyense wa inu molingana ndi ntchito zanu.

Ambuye atawonjezera madalitso Awo ku kuwerenga kwa Mawu Ake.

5 Samsoni, kuchita kwakukulu monga mpingo, anayambapo bwino. Iye anayambapo mu njira yolondola. Iye anayamba apo, ndipo ankatchedwa munthu wamphamvu zogonjetsa. Koma iye anayamba pa, kutumikira Ambuye, mwa kusunga Mawu Ake ndi kumachita Malamulo Ake. Ndipo izo zinali mwanjira ina monga mpingo. Izo zinayambika apo, monga ife tikanati tinene, monga kuyankhula kwa mdziko, anayamba ndi phazi lolondola. Anayamba kusunga Malamulo a Ambuye. Ndipo nthawi yonse pamene Samsoni ankawatsata Ambuye, Ambuye ankamugwiritsa ntchito Samsoni.

6 Pakuti, Mulungu akhoza kumusunga aliyense ndi kumugwiritsa ntchito aliyense yemwe angatsatire pambuyo pa Iye, pakuti ndi ntchito ya Mulungu. Koma pamene ife titembenukira kumbali, kuchoka ku zinthu za Mulungu, ndiye Mulungu sangakhoze kutigwiritsa ife ntchito mopitirizanso. Pamene ife tiyenda molimba potsata Malamulo a Mulungu,

pamene ife tikhala mu masamba a Baibulo ndi kupembedza mwa Mawu olembedwa, kumupembedza Iye mu Mzimu ndi mu Choonadi cha Mawu, ndiye Mulungu akhoza kumugwiritsa ntchito munthu aliyense. Koma pamene iwo atenga lingaliro loti atembenukire kumbali motsatira chinthu chinachake, ndiye Mulungu sangakhoze kumugwiritsa ntchito munthu ameneyo kenanso.

⁷ Koteru, Samsoni akupanga cho—choyimira chowoneka kwambiri cha mpingo lero. Pamene mpingo unayamba, Mulungu amakhoza kuwugwiritsa ntchito mpingo, pakuti mpingo un kayenda mosamalira potsatira Malamulo a Ambuye, unkasunga maweruzo Ake onse ndi malangizo Ake, ndi kuchita zonse za Malamulo Ake. Ndipo Mulungu anali nawo mpingo. Koma izo zikuwoneka kuti pali malo ofooketsa otero pakati pa mpingo.

⁸ Kumbukirani, ife sitiri pa masanje, koma ife tiri mu bwalo la nkondo. Anthu ambiri amangoganiza kuti pamene iwo akhala Mkhristu kuti ndicho chonse chimene iwo akusowa kuchita, kuti icho chimakhazikitsa izo kwanthawizonse, pamene iwo akhala Mkhristu kuti chirichonse chizingobwera mophweka. Musati konse mutengere izo mu mutu wanu. Pakuti, ine ndinakhala Mkhristu, kudzamenya nkondo, kudzamenya nkondo yabwibo ya chikhulupiriro. Ine ndinakhala Mkhristu kuti ndidzafike mu mizere ya nkondo. Ife ndife asirikali Achikhristu, ndipo ife tiyenera kuti tikhale ophunzitsidwa ndi oleredwa, ndi kudziwa machenjerero onse a mdani, kudziwa momwe tingalimbikitsire, kudziwa momwe tinga—tingamenyere nkondo. Ndipo ife tingakhoze kokha kuchita zimenezo pamene Mzimu Woyera uti uwululire izo kwa ife. Ife sitingakhoze kutenga zimene fuko lina likuti uza ife pamene ife tipita ku nkondo, ena a malingaliro awo. Koma ife tiyenera kutenga malingaliro athu athu, momwe Mzimu Woyera ukanati utitsogolerere ife ndi malingaliro amene Iye akanati atipatse ife, chifukwa Iye ali Mkulu Wolamulira wa nkondo ya Akhristu.

⁹ Samsoni anachita bwino, iye anali munthu wamkulu kufikira pamene iye anayamba, anayamba kukhala ngati (ife tingakutche iko) kupepera pamenepo, kufikira pamene iye anayamba kuchoka pa malire ake omwe. Ndipo mpingo unathamangadi bwino, ndipo unali bwino bwino mpaka pamene iwo anayamba kuchoka ku malire awo. Samsoni anayamba kudziyalutsa. Ndipo iye sanali kudziyalutsa ndi asungwana Achisraeli, iye anayamba kudziyalutsa ndi asungwana a Chifilisiti.

¹⁰ Ndipo ndicho chinachake chofanana ndi chimene mpingo unachita. Iwo sunayambe kupanga chikondi ndi ake ake, iwo unapita motsatira osakhulupirira ndi kuyamba kudziyalutsa ndi osakhulupirira. Ndi pamene ife tinapanga zolakwitsa zathu, zina zazikulu kwambiri, ndi pamene mpingo unayamba

kumachita zinthu zomwe sizinali zolondola. Iwo unayamba kumayenda nawo, monga Samsoni, amzake olakwika.

¹¹ Samsoni, monse pamene iye anali mu gulu la anthu a Ambuye, iye ankachita bwino. Koma pamene iye anayamba kudziyalutsa ndi amzake olakwika, ndiye iye analowa mu vuto.

¹² Ndipo ndimo momwe ziliri ndi mpingo. Pamene mpingo unkatsatira molemekeza tsiku ndi tsiku pambuyo pa kutsogolera kwa Mzimu Woyera, Mulungu ankawadalitsa iwo, ndipo zozizwitsa ndi zizindikiro ndi zodabwitsa zinkawutsatira mpingo. Koma pamene iwo unayamba kuyenda ndi gulu loyipa, ndi dziko! Chimodzi cha zinthu zoyipa chimene iwo unachita, ndi zinthu zoyamba zomwe iwo unachita, iwo unayamba kuchita bungwe, kuphwasula chiyanjano pakati pa okhulupirira ena, chifukwa iwo anapeza kuti mafuko anali kuchita bungwe. Koma Uthenga wawukulu uwu sunaperekedwe kwa fuko limodzi kapena anthu amodzi. Uli woperekedwa kwa “aliyense yemwe ati adzafune, msiyeni iye abwere,” mafuko onse, mitundu, malirime, ndi anthu. Mulungu sanalinge kuti ife tijambule mizere yathu ya malire.

¹³ Koma anthu ankafuna kuti akhale mofanana, iwo amafanizira, kapena kutengera za ena, kupita monga—dziko limachitira, kunena zinthu zomwe iwo amachita, kupanga kupambana momwe iwo analiri opambana. Ife sitingakhoze konse kukhala opambana pakuchita chirichonse chimene dziko limachita. Ife tingakhoze kokha kukhala opambana pamene ife titsatira malangizo a Mulungu ndi njira Yake ya kuchitira zinthu. Ife sitingakhoze konse kukhala, mwa kudziyerekeza motsatira dziko. Ngati kampani ya ndudu yapeza kupambana kwake kwakukulu pa televizioni, ndipo magulu amowa ndi a kachasu apanga kupambana kwawo kwakukulu kupyolera mu kuthandizira kwa televizioni, icho sindicho chizindikiro kuti mpingo udzapanga kupambana kwake ndi televizioni. Kupambana kwa mpingo kwagona mu kulalikira kwa Uthenga, wa Mphamvu ya Mulungu, ndi chiwonetsero cha Mzimu. Ife sitingakhoze kunena chifukwa kuti televizioni yachitira *zakuti-ndi-zakuti* kampane ya ndudu ndi ma—makampane ena! Ife tiribe Lemba lirilonse loti tiyesere kudziyerekezetsa ndi anthu amenewo. Ndipo monse pamene ife titero, ife tikhoza kukoka ziwerengero zazikulu za anthu, koma sindicho chimene Mulungu anatidzozera kuti ife tizichita. Ife timaganiza chifukwa ndife amitundu yonse, tikuwuluka pamwamba, mabungwe akuluakulu, kupangitsa zinthu zokongola kwambiri kuti zizichitika, kuti ndiko kupambana. Ife tikufa tsiku ndi tsiku tiri chiimire, kuyankhula mwauzimu! Ngati ife tikanayima mwamphamvu za mamilioni-khumi mmawa uno, ndipo Mzimu Woyera ukanati usakhale ndi ife, ife tikanachita bwino kuyima mwamphamvu za khumi ndi Mzimu Woyera uli nafe. Ife sitingakhoze kudzifanizitsa ndi dziko.

¹⁴ Ndipo chimodzi cha zinthu zoyamba, zinali, mpingo kuyamba kudzipanga wokha bungwe. Bungwe loyamba linali mpingo wa Katolika, ndiyeno kunadza mpingo wa Lutera. Pamene iwo anachita bungwe mu mpingo wa Katolika pa kuwupanga iwo bungwe, tsiku lina uko kunali kulira, “Afilisti ali pa iwe, Samsoni,” ndipo Samsoni anadula zingwe za nsinga za mpingo wa Katolika, ndipo Marteni Lutera anatulukira ndi bungwe.

¹⁵ Ndiye iwo anawumanga mpingo ndi chingwe china, monga Delila anachitira. Ndipo iwo anayamba...mmalo mokhala ndi munthu woyitanidwa ndi Mulungu, munthu yemwe anayitanidwa ndi Mzimu Woyera; mwina mwake osadziwa ma ABC awo, koma iwo amamudziwa Khristu. Ndiye mpingo unayamba mwa masitayilo, ndi kutengera monga oyankhula mwandale. Ndipo iwo anali kuwapatsa alaliki awo “digirii ya udokotala,” aliyense amayenera kukhala Dokotala Wauzimu. Icho chinali chingwe china choti awumangire mpingo. Anthu ankapita ndi kukaphunzira, seminare iliyonse kuyesera kutulutsa sikolala wabwinoko, kotero kuti mipingo yawo ikhoza kubwekerera, “M’busa wathu ndi Dokotala Wazauzimu.” Ndipo kodi iwo anachita chiyani? Wina amayesa kukhala nazo nzeru zochulukira kuposa mzakeyo. Chabwino, izo sizikutanthauza chirichonse pa maso pa Mulungu.

¹⁶ Ndipo palibe chosoweka kwa munthu aliyense kuti ayesere kutenga nzeru yachidziko yake ndi kumukondweretsa nayo Mulungu iyo konse. Ndicho themberero pamaso pa Mulungu! Inu simudzamukondweretsa konse Mulungu ndi zokhumba za chidziko ndi chidziwitso, chifukwa “ndizo udani kwa Mulungu,” limatero Lemba. Iye sangakhoze kuchita izo.

¹⁷ Ndipo aliyense amayesera kuti akhale nako kudziwa zonse. Iwo amadziwa basi choti achite ndi mawu oti awanene, ndipo izo zimangokhala kuyankhula kwandale basi mmalo mwa Uthenga wamphamvu wowonetsedwa, wa Mzimu Woyera umene umamira mu mtima wa munthu ndi kulipeza tchimo. Iwo amaphunzitsidwa za mayankhulidwe andale, ndipo ife sitikuzisowa zimenezo. Paulo anati, “Mawu amabwera kwa ife, osati kokha...kapena, Uthenga, mwa Mawu okha, koma kupyolera mu Mphamvu ndi chiwonetsero cha Mzimu Woyera.” Zimenezo zinkabweretsa Uthenga, kuwonetsera mphamvu za Mzimu Woyera! Koma anthu onsewa amapita ku maseminare ndipo iwo amakaphunzira maphunziro aakulu, momwe iwo ayenera kuyimira pamaso pa anthu, momwe iwo ayenera kudziperekera okha, momwe iwo ayenera kuvalira ndi momwe iwo ayenera kuchitira, iwo sayenera kugwiritsa ntchito galamala yolakwika. Tsopano, izo zonse nzabwino kwa kuyankhula kwa ndale, koma ife sitikutsatira mawu othyathyalika a munthu. Paulo anati, “Uthenga umene ine ndikulalikira sunabwere monga choncho, koma Iwo unabwera kupyolera mu kukonzanso

kwa—Mzimu Woyera ndi Mphamvu ya ziwonetsero.” Subwera mwa kayankhulidwe kokonzedwa bwino, koti nzeru yanu ingakhale, kapena kudalira kwanu kungakhale mu nzeru ya munthu. Koma iwo umabwera kupyolera mu kuwonetsera kwa Mphamvu ya Khristu wowuka. Ndiwo Uthenga, “Kumudziwa Iye mu Mphamvu ya chiwukitsiro Chake.”

¹⁸ Mmodzi aliyense amayesa kuganiza kuti iye ali wanzeru pang’ono kuposa munthu winayo, chipembedzo chirichonse. Amethodisti amati, “Ife tiri naye munthu wanzeru kwambiri.” Abaptisti amati, ndi mpingo wa Khristu, ndi ena otero, iwo onse, “Ife, ndife ophunzira kwambiri. Ife, athu—anthu athu, ife sitimangolola munthu wamba kupita kunja ndi kukalalikira Uthenga.” Koma iwo amachita kuwasankha iwo. (O Mulungu, chitani chifundo!) Kuchita kuwasankha iwo; ngati iwo ali omwela pa chiphunzitso chawo chinachake, ndiye iwo amawayika iwo mu mpingo. Mulungu sangakhoze kumukhudza iye mwanjira iliyonse. Ine ndikufuna winawake kuti azilalikira kwa ine yemwe anachita kusankhidwa ndi Mzimu Woyera, Mulungu wamuwukitsa, osati kusankhidwa ndi munthu kapena zipembedzo.

¹⁹ Onse anzeru! Iwo amati, “O, ife tikudziwa zonse za Izo,” ndipo ena a iwo sadziwa alifabeti yoyamba ya Mzimu Woyera. Iwo amawukana Iwo.

²⁰ Izo zikundikumbutsa ine za kabukhu kakang’ono kamene ine ndinawerenga tsiku lina mu California, pafupi zaka khumi zapitazo. Ine ndinalitenga ilo mu nyumba yamabuku yakale. Ine ndayiwala yemwe anali mlembi wake. Bukhu la masenti-khumi chabe, koma ilo linali ndi lingaliro lina labwino kwa ilo ngakhale zimawoneka mwanthabwala ndi mothyathyalika. Koma, ine ndinapeza chinachake mkati mmenemo chimene chinamveka ngati Mulungu, kwa ine. Ndipo imodzi ya tinkhani tating’onoto inayamba monga chonchi. Mmawa wina mu khola lalikulu la nkuku, munali tambala wamng’ono winawake amene ankaganiza kuti anali nako kudziwa konse kumene kunalipo koti kudziwidwe. Kotero iye anawulukira pa bokosi kumenyetsa mulomo wake wawung’ono pa bokosipo, nthawi zinai kapena zisanu, kuponyera mmbuyo mutu wake wawung’ono ndi kulira monga inu simunayambe mwamvapo tambala akulira. Ndipo enawo, iye anawakopa tcheru chawo, ndipo iye anati, “Madona ndi mabwana a khola ili la nkuku, ine ndikufuna kuti ndiyankhule kwa inu nonse mmawa uno pa dongosolo lina la maphunziro limene ife tangolikonza kumene.” Anati, “Ine ndapeza nzeru zochuluka mu kuphunzira kwanga,” pamene iye anali kukokera mandala ake aang’ono pamwamba pa mulomo wake. Ndipo iye anati, “Ine ndalingalira kuti ife nkuku tikhoza kudzipezetsa bwino ifeeni ndi nzeru zochuluka. Chotero, ine ndikhoza kukuuzani inu kumene kuli, ngati ife tikanakakumba ndi kugwira ntchito mu khola linalake kapena dzenje, ife

tikapeza vitamini inayake yomwe iti idzatipangitse ife kulira bwinoko, nthenga zabwinoko. Ndipo, o, ine ndikhoza kukuuzani inu momwe ife tingakhoze kudzitukula tokha mu njira zambiri zosiyana.”

²¹ Ndipo tianapiye tating’ono ta malitchowa awo aang’ono ofiira, ito basi tinangosekelera ndi kuti, “Kodi iye si wokondeka?” Ndipo iwo ndithudi anamusilira iye. “O, iye ndi tambala waluntha chotero!” Zikundikumbutsa ine za ena mwa awa kuno alaliki a ku seminare. “Munthu wanzeru chotero! Palibe kufunikira kuti ife tizikhala pozungulira ndi nkuku zinazo, ife tonse tikuyenera kupita ndi iye.”

²² Chabwino, kanthu kakang’onoko katsanatsirize kuyankhula kwake, apo panali kankhuku kena kakang’ono kamene kanalibe nthenga zokongola chotero, kanabwera chothamangira mkati kuchokera ku khola la nkuku zonsezo, ndipo kanati, “Anyamata, miniti chabe! Ine ndangomva nkhani zaposachedwapa pa wailesi. Nkhuku zakwera masenti anai pa libisi, ife tonse tikupita kokazingidwa mawa! Kodi nzeru zanu zichita ubwino wanji?”

²³ M’bale, kudziwa konse kumene ife tingakhoze kudziunjikira, kodi kungachite ubwino wanji? Ndife mapazi asanu ndi limodzi a fumbi! Ife tonse tikufa mwa mainchesi ndi mwa maminiti. Kudziwa kwathu sikutanthauza kanthu. Ife tikusowa kumudziwa Iye. Koma iwo amachita zimenezo.

²⁴ Monga ine ndinali kuchitira ndemanga nthawi yina pa kale zokhudza chingolopiyo wamng’ono winawake ndipo iye ankaganiza kuti iye ankadziwa nzeru zonse zimene—zimene ziyenera kudziwidwa, ndipo iye ankadziwa zochuluka kwambiri mwakuti iye ankakhoza kuwauza achingolopiyo zonse zokhudza anthu. Chotero amaulukira mmwamba pa chisa chake nayamba kulankhula za munthu, momwe amadziwira zonse za iwo. Ndipo, zonse mwadzidzidzi, puofesara wochokera ku Purdue anayimirira nayamba kulankhula mawu ena opukutidwa-mwapamwamba kwa iye, ndipo wamng’ono anaphethira maso ake natembenuza mutu wake. Tsopano, iye anali nawo maso, iye amakhoza kumupenya puofesara. Iye anali nawo makutu, iye amakhoza kumumva iye. Koma, ndithudi, iye sankadziwa chimene iye anali kuchikamba. Chifukwa chiyani? Iye ali nawo ubongo wa chingolopiyo. Iyo yangokhala mbalame yaubongo basi. Ndizo zonse zomwe iye ali nazo. Iye alibe ubongo waumunthu, kotero iye sangakhoze kuganiza monga anthu.

²⁵ Ndipo ngakhalenso munthu sangakhoze kuganiza monga Mulungu! Ndiwe munthu, ndipo nzeru zonse zachidziko siziri zochuluka kuposa ubongo wa chingolopiyo. Zonse zomwe iwe umachita, iwe umangozipweteka wekha ndi izo. Iwe uyenera kukhala nalo lingaliro la Khristu.

²⁶ Chifukwa chimene anthu amapita ndi kukajowina mabungwe, ndi kulowetsamo kugwirana chanza mmalo mwa kubadwa kwatsopano, iwo akuyesa kulambalala kubadwa kwatsopano. Iwo sakukufuna kubadwa kwatsopano. Ndipo iwo—iwo akudziwa kuti ife timaphunzitsa izo mu Baibulo, kotero iwo akufuna kuti alowetsemo chinachake mmalo mwa iko. Ndipo anthu Achipentekoste ali oyipa chimodzimodzi basi, pakuyesera kulowezamo chinachake! Iwo akufuna izo mwapamwamba. Izo ziyenera kungokhala mwapamwamba chotero, “Ife tizigwirana manja ndi kujowina mpingo, ndi kukonkhedwa kapena kubatizidwa,” kapena chinachake. Iwo akuwopa kubadwa kwatsopano. Ine nthawizina ndimakhulupirira kuti Branham Tabernacle ikukuwopa iko!

²⁷ Tsopano, ife tonse tikudziwa kuti kubadwa, ine sindikusamala kumene iko kuli, kapena kuti, malo ake, ndi nyansi. Ngati mwana wabadwa pa mulu wa mankhusu, pansu polimba, kapena mu chipinda chokongoletsedwa mwa pinki ku chipatala, ndi nyansi, mulimonse. Kubadwa kwa ng’ombe, kubadwa kwa china chirichonse, ndi nyansi.

²⁸ Ndipo kubadwa kwatsopano sikuli kanthu kochepera kuposa nyansi! Koma anthu akhuthara kwambiri, “Ife tipita kumene amagwirana chanza. Ife tipita kumene iwo samazazira ndi kulira, ndi kumenya pa guwa ndi kufuula.” Inu mukufuna kukhala waumunthu kwambiri! Chimene ife tikusowa ndi kubadwa, kufapo, kumene kumabadwitsa moyo.

²⁹ Mbewu, mbatata yakale, mbewu ya mbatata, inu mukatenga mbatata imeneyo ndi kuyiyika iyo mu nthaka. Mpaka pamene inu mungakhale ndi mbatata zatsopano, mbatata yakaleyo iyenera kuvunda. Chimanga sichingakhoze kubala moyo watsopano mpaka icho chitavunda.

³⁰ Ndipo mwamuna kapena mkazi sangakhoze konse kukhala ndi kubadwa kwatsopano mpaka za luntha zawo ndi zaumwini zawo zitavunda, zitafa, kufera pa guwa, ndi kukuwa, kudzifikitsa yense ponyansiratu, mpaka pa malo omwe kukhuthara kungachoke pa kolala yako, ndipo ndiwe wobadwa kachiwiri mwa Mzimu wa Mulungu. Ine sindikusamala kaya iwe ukuwa, kuyankhula mu malirime, kulumpha mmwambandi-pansi, kuwuluka ngati nkhuku mutu wake utadulidwa, iwe ukubadwitsa Moyo watsopano! Koma ife timalowezapo chinachake mmalo mwa iko, ife tikufuna njira ya yapamwamba, zedi.

³¹ Tsiku lina, Lachisanu, mkazanga ndi ine tinali kupita ku sitolo. Ine sindikutanthauza kukhalitsa pa izi. Koma pamene ife tinali kupita chotsika ndi msewu, ine ndimangopitirira kupotolozera mutu wanga kuchokera mbali imodzi ndi ku inzake, akazi amaliseche. Ine ndinamulonjeza Mulungu pamene ine ndinali munthu wakhungu, ngati Iye akanati achize maso

anga ine ndikanati ndiziyang'ana pa chinthu chimene chinali cholondola. Ndipo ine ndimasunga ka mtanda kakang'ono katapachikika mu galimoto yanga. Pamene ine ndiwona zotero zonga zimenezo, ine ndimayang'ana pa mtanda ndi kuti, "O Mulungu, Ndipo Pothawirapo panga," pamene ine ndiyang'ana pa mtanda.

³² Ine ndinawaona akazi amenewo. Meda anati, "Ife sitinamuwone mkazi mmodzi lero yemwe wavala siketi." Ndipo iye anati, "Bill, tayang'ana pa mkazi uyo apo ali ndi zomangira zimenezo mozungulira mu mtunda mwa thupi lake," ndipo anati, "iwe ukutanthauza kuti undiuze ine kuti mkazi ameneyo sakudziwa kuti izo ndi zolakwika?" Anati, "Ngati iye sakudziwa kuti izo ndi zolakwika, ndiye iye wachoka ku malingaliro ake abwino."

³³ Ine ndinati, "Miniti yokha, wokonedwa. Iye ndi Mmereka, iye amachita monga Achimereka amachitira." Ine ndinati, "Ine ndinali mu Finland osati kale lapitalo, wokonedwa."

³⁴ Ndipo ine ndinamufunsa kumeneko mwamuna yemwe anandikhazika ine pansu, Dokotala Manninen. Ndipo ife tinali kupita ku—kokasamba mwaukhondo, komwe kumatchedwa sauna, ndipo iwo amakutengera iwe mkati ndi kutsanulira madzi otentha, kapena madzi pa miyala yotentha, ndipo iwo basi amangokuchititsa thukuta iwe. Ndiye iwo amakupangitsa iwe kudumphira mu madzi a chisanu, ndiyeno nkukuchotsamo. Ndiye amakutengera iwe kupita mchipinda, ndipo umo muli anamwino mmenemo, akazi amene amawakhula amuna (ndipo iwo ali maliseche), nkuwatumizanso iwo kupita mu dziwe. Ine sindikanapita mmenemo. Ndipo ine ndinati, "Dokotala Manninen, izo ndi zolakwika."

³⁵ Iye anati, "Chabwino ndiye, M'busa Branham, izo ndi zolakwika. Ndiye nanga bwanji madokotala anu Achimereka omwe angamuvule mkazi maliseche ndi kumugoneka iye pa thebulo, kumupima chiwalo chirichonse—chiwalo chogonerana chimene iye ali nacho? Nanga bwanji anamwino anu mu zipatala?"

³⁶ Ine ndinati, "Mundikhululukire ine, M'bale Manninen, Manninen, inu mukulondola."

³⁷ Ndi chiyani chimenecho? Ndi miyambo. Pamene ine ndinali mu Paris ine sindimakhoza konse kukhulupirira izo, kuti mokodzera mwa onse amuna ndi akazi munali mumodzi momwemo. Ine sindimakhoza kumvetsa izo, kuti zimbudzi zinali mu mbali ya msewu kwa onse amuna ndi akazi. Ine sindimakhoza kukhulupirira kuti pamene akazi amapita ku doko kuti akasambire, mnyamata ndi wokoma mtima wake, iwo analibe zipinda zovaliramo, iwo amangovula zovala zawo zonse mpaka ku chovala chotsiriza, ndiye nkutembenezirana misana yawo ndi kuvala kachingwe kakang'ono ndi kumapita

nasambira, koma ziri chomwecho. Iwo sapereka chidwi kwa izo. Ndiwo mwambo waku France.

³⁸ Mu Afrika, akazi ndi amuna, aang’ono ndi aakulu, opanda zovala nkomwe, akuyenda kupyola mminda. Osadziwa nkomwe chomwe chimbudzi chinali, kapena zinthu, kapena osabisala kwa wina ndi mzake. Koma iwo sadziwa kusiyana. Iwo sakudziwa kusiyana. Koma ndiyo miyambo ya mafuko.

³⁹ Koma ine ndinati, “Wokonedwa, ife ndife osiyana, ndife ochokera ku Fuko lina. Ife ndife amwendamnjira ndi alendo kuno, ndicho chimene chimapangitsa zinthu zimenezi kuwoneka zolakwika chotero. Pakuti Baibulo linati, ‘Iwo amene amadzinenera zoterozo, amadzinenera, iwo amasonyeza kuti iwo ali amwendamnjira ndi alendo, iwo akufunafuna mzinda wakudza.’”

⁴⁰ Mwamuna kapena mkazi mu Italy, mu France, mu Africa, mu fuko lina lirilonse, yemwe anayambapo wabadwa kachiwiri ndi Mzimu Woyera, samachita zinthu zimenezo. Iwo sangamavale zovala zimenezo. Iwo sangamachite monga chomwecho, chifukwa iwo ali a Fuko lina lomwe Wolamulira Wake ndi Wolipanga ali Mulungu. Ndife ochokera Kumwamba. Mzimu umene uli mkati mwa inu, umalamulira moyo wanu. Ngati iwe uli Wachimereka, iwe uzichita monga Achimereka amachitira. Ngati iwe uli wa Chifransa, iwe uzichita monga Achifransa amachitira, ndi kumamutsutsa mmodzi wina. Koma ngati ndiwe wa Mulungu, iwe uzichita momwe iwo amachitira Kumwamba, chifukwa Mzimu wako umabwera kuchokera Kumwamba ndipo Iwo umakulamulira iwe.

⁴¹ Chinachake chaching’ono chimene inu mungakhoze kuyang’anapo. Mu Lemba, iwo amene ankafuna Mzinda watsopano uwu, ankachita mosiyana. Iwo ankadzinenera kuti iwo anali amwendamnjira ndi alendo. Koma ku mbali ya Kaini, iwo anakhala obisalira ndi zigawenga. Koma Akhristu anali amwendamnjira ndi alendo. Obisalira samakhala nako kwawo, chigawenga ali munthu woyipa. Koma mwendamnjira ndi chinachake chenicheni, ndi wochokera ku dziko lenileni mu Fuko lina, akuyesera kuti apeze njira yake ya Kwawo, kudzinenera mwa kukhala kwake kuti iye ali nacho chinachake choti iye ndi wochokera ku Dziko lina. Chimenecho ndicho chifukwa chake.

⁴² Komabe anthu awo amene amachita zimenezo, anthu amenewo amene amavala zinthu zimenezo, ndiroleni ine ndikuuzeni inu. Mu South Afrika, pamene ine ndinawona zikwi makumi atatu achikunja aawisi, amaliseche, anthu ovala bulangeti. Khumi ndi zisanu ndi chimodzi, khumi ndi zisanu ndi zitatu, asungwana a zaka-makumi awiri zakubadwa, anyamata opanda ulusi umodzi wa zovala, atayima pamenepo ali ndi matope mu nkhope zawo, ndipo atazilocha, mafupa

atawalowetsa mu mphuno zawo, ndi zidutswa za mtengo zikulendewera pa makutu awo, ndi kupachika mafupa a anthu kapena mafupa ena mu tsitsi lawo, mano a zinyama atapachikidwa pa iwo, amaliseche monga iwo anabwerera mu dziko, ndipo sanali kudziwa izo. Koma pamene iwo analandira Khristu, ndipo anagwa pa nkhope zawo ndi kulandira Mzimu Woyera, iwo anawuka ndipo anapinda mikono yawo kuti agwire manyazi ku chifukato chawo, pamene iwo anali kuchokapo ndipo anapeza zovala zoti avale. Chifukwa chiyani? Iwo anakhala amwendamnjira ndi alendo ku dziko lino. Aleluya! Iwo anali kutali kwa Iye. Inde, bwana.

⁴³ O, inde, anthu awa amene amadzitcha okha Akhristu. Iwo ali mu mipingo. Iwo amachokapo ndi kumati, “Ife ndife Amethodisti. Ife ndife Abaptisti. Ndife Apentekoste. Ndife a Seventh-day Adventists. Ndife *ichi, icho*, ndi *chimzake*.” Icho chiribe chinthu chimodzi chochita ndi izo. Mzimu wako, moyo umene uli mwa iwe, umakulamulira ndi kukuuza iwe chimene uli. Yesu anati, “Ndi chipatso chawo inu mudzawadziwa iwo.”

⁴⁴ Mpingo wakhala monga Israeli, poyamba. Iwo ankawona mafuko onse achikunja ali nayo mfumu. Mulungu anali Mfumu yawo. Ndipo iwo anawaona mafuko achikunja ali nayo mfumu, kotero iwo ankafuna kuchita monga mafuko achikunja, ndipo iwo anadzigulira mfumu yawo. Ndipo pamene iwo anachita izo, iwo analowa mu vuto. Pang’onopang’ono izo zinayamba kulowa mkati. Pang’onopang’ono dziko linayamba kulowerera pakati pa iwo. Potsiriza zinathera mwa Ahabu. Mfumu imodzi ikubwera moyandikira pang’ono chabe kwa izo, moyandikira pang’ono kwa iwo, ndipo potsiriza kufinya moyo kuchokera mwa iwo. Ndipo apo iwo anapita. Ndipo pamene Mfumu yeniyeni inabwera, iwo sanamudziwe Iye.

⁴⁵ Ndicho chinthu chomwecho chimene mpingo wachita. Iwo watengera. Ndinu pano. Iwo watengera ndale, maphunziro. Iwo watengera mabungwe, gulu, mipingo yayikulu, alaliki odzitukumula. Ndipo pamene Mfumu yeniyeni wabwera, iwo sakumudziwa Iye, ndipo iwo akupachika Mzimu Woyera amene yemwe ali Mfumu yawo. Iwo sakumudziwa Iye, koma iwo amaseka pa Iye ndi kumuseleula Iye. Monga Ayuda anachita naye Mesiya wawo, mpingo ukuchita naye Mesiya wawo mwanjira yomweyo. Iwo sakudziwa zimenezo. Iwo alibe kupenya kwamkati kwauzimu, chifukwa iwo ali omwera kwambiri ndi maso awo ndi zimene iwo amawona, nyumba zazikulu, kuyesera kudzifanizitsa ndi dziko. Ife sitiri konse kukweza—kukwezedwa kuti tikafanene ndi dziko. Ife tikukwezedwa kuti tidzichepetse tokha.

⁴⁶ Ndipo, mmodzi ali chigulu, mwa Mulungu. Ndipo lero mu uvangeri wa machiritso kunja mminda, kuli mpikisano woterowo, opikisana. Mmodzi amati, “Chabwino, nkudalitsa Mulungu, ine ndiri nawo zikwi zambiri choncho. Ine ndiri

nawo msonkhano waukulu kuposa womwe inu muli nawo.” Zimapanga kusiyana kotani zimenezo? Ife tikakhala naye mmodzi kapena milioni imodzi, zimapanga kusiyana kwanji izo? Kodi ndife owona kwa Mulungu? Kodi ndife owona kwa Mawu Ake? Kodi ife timayima pansi pa kuyesa kwa Mzimu Woyera? Kodi izo nzoona? Ndicho chinthu chachikulu.

⁴⁷ Koma ife timanyengerera pa Baibulo. Ambiri a anthu athu Achipentekoste, pa Ziphunzitso za chikhazikitso za Baibulo ili, amanyengerera. Pali...ine sindikufuna kuvulaza kumverera. Ine ndiri mu mpingo wanga womwe, ndipo ine ndikumverera kuti ine—ine ndikhoza kuchita basi chimene, mu mpingo wanga, chifukwa ine ndikulalikira Uthenga. Koma alipo makumi a zikwi a alaliki Achipentekoste amene amadziwa kuti palibe chinthu choterocho mu Baibulo monga ubatizo mu dzina la “Atate, Mwana, Mzimu Woyera.” Ine ndikuwatsutsa a alikibishopu, kapena aliyense, kuti andisonyeze ine pamene wina aliyense anayamba wabatizidwapo mu dzina la “Atate, Mwana, Mzimu Woyera.” Koma iwo amanyengerera, chifukwa mabungwe achita chotero. Palibe munthu mmodzi mu Chipangano Chatsopano, ndipo kwa zaka mazana atatu mtsogolomo, mwa mbiriyakale, kupatula yemwe anabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu. Ndi chiyani chimenecho? Bungwe. Ndilo linachita izo. Kunyengerera!

⁴⁸ Ndipo lero iwo atenga onse ogwira ntchito mu msewu kuwachotsa mmisewu. Iwo achotsamo nkhocho mu mpingo. Iwo achotsamo ulemere wonse mu mpingo, ndipo atenga kulalikira kwa chiseminare, kulalikira kwa kupesa kwakale pang’ono kwa tambala, onse opukutidwa mu gululo, ndipo akazi awo kumavala akabudula ndi madiresi omwe iwo amafinyidwiramo, ndipo amuna kumasuta ndudu, ndi kuchita njuga ndi kumanena nthabwala zonyansa. Ndicho chamanyazi pamaso pa Mulungu! Ine ndikudziwa kuti izo ndi zamwano, koma ndi nthawi yoti winawake anene chinachake. Kunyengerera, kugonjera, kumachita monga dziko!

⁴⁹ Ine sindikusamala ngati ine ndichita kuyima ndekha, popanda wina koma Mulungu yekha, ine ndizilalikira Choonadi cha Baibulo la Mulungu ndi kuyima nacho Icho. Ngati ine nditafe, ine ndidzayimirabe Choonadi. Ndithudi. Ife tikufuna Choonadi. Ine ndidzaziyeza osati molingana ndi mpingo, koma molingana ndi Mawu a Mulungu ine ndikufuna kuziyeza nawo.

⁵⁰ Koma Delila, kodi inu munazindikira, iye ankadziwa kuti Samsoni anali nayo mphamvu. Ndipo iye sankadziwa kumene mphamvu imeneyo inagona. Iye sankakhoza kudziwa chimene mphamvuyo inali, koma panali mphamvu yina yayikulu imene Samsoni anali nayo, ndipo iye ankafuna kuti ayipeze iyo. Ndipo, monga Delila, iye anapitiriza kumamunyengerera Samsoni potsatira kukongola kwake. O, iye anadziveka yekha mwa chigololo kwenikweni. Ndipo iye ankayenda pamaso pa iye

ndipo iye ankati hede monga ena a ang'ono a zaka zopitirira khumi a tsikuli, ndi—ndi zina zotero, ndipo akufuna azingochita monga china chimzake, wodolola podzivula, kuyesera kuti amukopere Samsoni kwa iye.

51 Ndicho chinthu chomwecho dziko lachita kwa mpingo. Tsopano kodi Mphamvu yanu yaikulu ili kuti?

52 “Chabwino, ngati ife titachite bungwe, zimenezo zidzaiphwasula Mphamvuyo.” Mpingo wa Katolika unachita zimenezo.

53 “Koma Afilisti ali pa iwe, Samsoni.” Ndipo Lutera anatulukira.

54 Ndiye iwo anachita bungwe kachiwiri. “Ngati iwe uti undimange ine ndi chingwe china, icho chidzandigwira ine.” Kotero iwo anatero.

55 “Ndipo Afilisti ali pa iwe, Samsoni.” Nchiyani chinachitika? Wesile anatulukira ndipo anadula zingwezo.

56 “Tsopano iwe wandinyenga ine motalika konseku. Kodi iwe sukudziwa kuti ine ndimakukonda iwe, Samsoni? Chabwino, ndiye ine choonadi cha mu mtima wako.”

“Chabwino, iwe undimange ine ndi chingwe china.”

57 “Chabwino, tsopano ife tichita zimenezo.” Ndi chiyani chimenecho? Ndicho chingwe cha chipembedzo.

58 “Inu mundisiye ine ndikhale mfulu, kuti ine ndisakhale chipembedzo. Ndiye, ine ndikuuzani inu, inu mufika pondiphwasula ine.” Kotero kunatulukira Achipentekoste. Ili kuti Mphamvu yako?

“Afilisti ali pa iwe.” Ndipo iye anadula zingwezo kachiwiri.

59 Koma tsopano nchiyani chinachitika? Izo zawapezeketsa Achipentekoste, Madokotala Auzimu aakulu kuti akhale azibusa awo, munthu wina wamkulu. Iwo ali nako kuphunzira kochulukira basi ndi mwambo monga Amethodisti kapena Abaptisti, kapena aliyense wa iwo onse ali nazo. Kupita mu mpingo ndipo iwe sungakhoze kumva “ameni,” ozizira basi monga gulu la Maeskimo komwe uko ku Mapeto a Kumpoto. Ozizira! Osayanjanitsika! “Ndipo tsopano Afilisti ali pa iwe, Samsoni.”

60 Afilisti ali pa iwe, Amereka. Uli kuti umodzi wa mzimu uja? Uli kuti umodzi wa Chipentekoste? A Assemblies of God, ndi a United, ndi mpingo wa Mulungu, ndi *izi, izo, zimzake*, aliyense ali nalo lingaliro losiyana, mmodzi uyu ndi *ilo*, ndipo mmodzi uyu ndi *ilo*. Ndifitse oswedwa kwambiri mpaka iwe ukhoza kupita mu mzinda kukachititsa chitsitsimutso, ngati mpingo umodzi uthandizira icho, ina yonseyo siyikakhalako ngakhale. Achikominsi ali pa iwe, Amereka.

61 Mphamvu yathu ili pati? Ulemerero wathu uli kuti? Ndi chiyani icho? Chifukwa ife tinatsatira nzeru ya munthu mmalo mwa Mphamvu ya Mulungu! Bwanji, iwo awapangitsa alaliki athu ndi zinthu zowuma ndi zokhuthara, mpaka iwo atipanga ife bungwe mpaka ife tiri okhuthara kwambiri ndi owumamakosi, mpaka anthu... Kodi inu mukumamva konse kufuula mu mpingo panonso? Iwe sumamumva aliyense akulira. Mpando wa obuma wayikidwa mchipinda cha pansu. Mulibenso ulemerero mu mpingo. Zonse zimene ife timachita ndi kukhala kumbuyo basi okhuthala monga ife tingakhoze kukhalira. Si ndife afulu. Ndife omangika. Mdierekezi, ndi ziwanda zake zamakono, zaumanga mpingo wa Mulungu wamoyo. Ndiko kulondola. Mulibenso Mphamvu mu mpingo. Mulibenso ufulu. Anthu ndi okhuthara ndi owuma! Bwanji, Mulungu akhoza kubwera mkati mwa anthu Ake Achipentekoste, ndi kuwasonyeza kuti Iye ndi Mulungu, ndi kutsimikizira zizindikiro za chiwukitsiro Chake, izo sizimawagwedeza iwo nkomwe. Ulemerero! Bwanji, ndicho chamanyazi! Ine ndimayenda kudutsa dziko lonse, Mulungu akugwira ntchito, akuchita zizindikiro, ndipo anthu nkukhala, ndi, “Chabwino, ine ndikuganiza ndizo zabwino. O, ine ndikudziwa izo zikhoza kuchitidwa.” Izo sizimawasuntha iwo! Chifukwa chiyani? Iwo amangidwa ndi Delila, dziko. Iwo ali mu zingwe.

62 Tsopano iwo awatengera iwowo ngakhale mkati, kuwamangira iwo mu chitaganya. “Afilisti ali pa iwe, Samsoni.” Iwe uchita chiyani pa zimenezo?

63 “O, ife tiri nazo zipembedzo zazikulu.” Zedi. “Ife tiri nawo mamembala aakulu kuposa momwe tinayamba takhala nawo.” Koma Mzimu uli kuti? Mzimu Woyera uli kuti?

64 Ndicho chimene Mdierekezi wachita. Iye wawanyengerera kulowa mu mpingo. Iye wakhala akuunyengererabe mpingo, “Bwerani kwa ine, ine ndikupatsani inu kachisi wamkulu kwambiri apa ngati inu muti muzingochita *izi*. Ngati inu muti mungomuchotsa mlaliki wotentheka uyo yemwe inu muli naye, ndi kupeza mwamuna, ali Dokotala wa Uzimu yemwe ali nazo nzeru zina, ife tidzamanga tchalitchi china chabwino chachikulu chapamwamba ndipo ife tidzakhala monga ena onsewo.” Manyazi pa inu! Kuli bwino ndikhale ndi munthu yemwe samadziwa kulekanitsa khofi woswedwa ndi nyemba, koma ali wodzazidwa nawo Mzimu Woyera, yemwe ali wosanyengerera, ali nayo Mphamvu ya Mulungu.

65 Koma izo zafika, o, mokhuthara kwambiri, mpaka woyera wina wosauka akhoza kulowerera mu msonkhano ndi kuyankhula mu malirime, kapena kufuula pang’ono pokha, kapena kuchita chinachake, ndi onse a iwo nkumanyumwa pozungulira ndi kuyang’ana. “Chinali chiyani chimenecho? Chabwino, mukudabwa chiyani? Uyo ayenera kuti wotentheka analowerera mkati penapake.” Inu mukudziwa kuti izo ndi

zoona! Woyera wina wosauka akalowa mkati, akayamba kukondwa mokwanira kuti akweza manja ake, ndi kumalira ndi kumayamika Ambuye, winawake yemwe angati afuule “ameni” ku kulalikirira kwa Uthenga, ndipo ena onse a iwo amatembenuka pozungulira kuti akawone chimene iye ananena. Awo ndi Achipentekoste. Chavuta ndi chiyani? Inu mukutengera za Amethodisti, mukutengera Abaptisti; iwo anatengera za Katolika; Katolika anatengera za ku gehena. Ndipo, zonse palimodzi, izo zonse zikutengera gehena! Kulondola.

⁶⁶ Delila wakunyengererani inu kupita mu mipingo yayikulu, yabwino, atumiki ophunzitsidwa, kutenga kalasi labwino. “Chabwino, inu mukudziwa, *Wakuti-ndi-wakuti* kumusi uko ndi milioneya, ngati ife titangomutengera iye kuti abwere mu gulu lathu! O, mai!” Ngati iye sali wobadwa kachiwiri, ndiye iye sakuyenera kukhala ali kumeneko. Ine sindikusamala ngati iye ali ndi madola milioni. Ngati iye ali ndi Makadilaki makumi anai, chirichonse chimene iye ali nacho, iye ayenera kubadwa kachiwiri, kubwera kumusi kumene ku kubadwa kwatsopano ndi kusinthidwa mwa Mzimu Woyera, ndi kubwera kuchokera uko mu kubadwa kwatsopano, mamina (mundikhulukire ine), akulira ndi kukuwa, ndi kumapitirizabe monga ena onsewo amachitira, ndi kukhala moyo kenako woti uzitsimikizira kuti iye ali nawo Iwo. Ameni. Ndicho chimene inu mukusowa.

⁶⁷ “Samsoni, Afilisti ali pa iwe.” Achikominsi ali pa iwe. Dziko liri pa iwe. Mdierekezi ali pa iwe.

⁶⁸ Iwo amapita mmbuyo ndipo iwo amawona Mzimu wa Mulungu ukuchita zozizwitsa ndi kuchita zinthu za chiwukitsiro Chake, zomwe Yesu analonjeza, iwo amati, “Inu mukudziwa, ine ndikuganiza M’bale Branham ali nako kuweringa maganizo kuchuluka. Abusa anati izo zinali za Mdierekezi.”

⁶⁹ Iwe wosauka wachinyengo, wodedeluka, wachikunja, wopukutidwa yense, iwe nkhandwe mu zovala za nkhusa! Yesu anati, “Ngati inu mukanandidziwa Ine, inu mukanalidziwa tsiku Langa.” Koma inu muli nawo mulu wa a Sauli amene amayesera kukupangani inu monga dziko lonse.

⁷⁰ Ife tikufuna gulu la anthu a Mulungu amene sanyengerera pa Mawu, koma kulalikirira Choonadi ndi kuyima pa ubatizo wa Mzimu Woyera.

⁷¹ Koma kodi dziko lachita chiyani? Ilo lameta Mphamvu zanu zonse. Iwe unabadwa uli Mnaziri, Pentekoste, koma dziko ndithudi lakumeta Mphamvu yako. Tsopano ndinu okhuthara basi monga ena onsewo.

⁷² Kodi ife tichita chiyani? Nchiyani chiti chichitike? Pali chinthu chimodzi chaulemerero chimene ine ndingakhoze kuchilingalira ku mapeto a nkhani iyi.

⁷³ Pamene Samsoni anali atamangidwa! Ife sitingakhoze kukhala nacho chitsitsimutso. Mvetserani pa m’bale wathu

wodzipereka, Billy Graham, “Chitsitsimutso mu tsiku lathu!” Tamvetserani pa Oral Roberts akukuwa, “Chitsitsimutso mu tsiku lathu!” Mvetserani pa ena onsewo a iwo, “Chitsitsimutso mu tsiku lathu!” Ife tingakhoze bwanji kukhala ndi chitsitsimutso pamene ife tamangidwa? Ife taumanga Mzimu Woyera, ndi mabungwe athu ndi miyambo, ndipo ife sitingakhoze kukhala nacho chitsitsimutso cha Mzimu Woyera. Ameni. Ine ndikudziwa kuti zimenezo zikuwawula motantha, ndi nyengoyi, koma ndicho Choonadi. Ife tingakhoze bwanji kukhala nacho chitsitsimutso cha Mzimu Woyera pamene inu muli omangidwa chotero ndi okhuthara! “Mawonekedwe aumulungu,” Baibulo linati iwo akanadzakhala nawo. “Mawonekedwe aumulungu, koma akanadzakana Mphamvu yake.” Mphamvu ya chiyani? Mphamvu ya bungwe? Mphamvu ya dziko? Mphamvu ya mpingo? Mphamvu ya Mzimu Woyera! Ndiwo malo achinsinsi mu mpingo. Ndipo pamene mpingo utenga alaliki ophunzitsidwa, ndi nyumba zazikulu ndi zokongola, mmalo mwa Mzimu Woyera wakachitidwe kachikale, iwo kulibwino akhalenso mu mishoni kachiwiri. Ameni. Zoonadi. Inu mukhala nacho bwanji chitsitsimutso cha Mzimu Woyera, ndipo anthu akuwuziziritsa Iwo ndipo akuwumanga Iwo ndipo alikuwuwopa Iwo? Apo ndi pamene pagona vuto.

⁷⁴ “Afilisti ali pa iwe.” Koma chiyembekezo chimodzi chodala chimene ife tiri nacho, pamene Samsoni anali mu ndende . . .

⁷⁵ Chinthu choyamba ndi chiyani chomwe iwo anachita pamene iwo anamugwira iye? Iwo anamumanga iye, choyamba. Iwo anachotsa mphamvu yake, iwo anapeza chinsinsi chake. Iwo anapeza chinsinsi chanu. Dziko linapeza chinsinsi chanu. Tsopano inu akazi nonse mumadula tsitsi lanu, izo zikupita monga dziko. Inu amuna nonse mumapita ndi kukachita monga dziko. Izo zonse ndi zabwino, kunena nthabwala ndi nthabwala zauve, ndi kutuluka panja ndi kukasuta ndudu zingapo ndi kuthawitsana ndi azikazi a oyandikana nawo, ndi china chirichonse monga choncho, kachakumwa kakang’ono kosangalatsa kuti mukhalebe pa ntchito yanu. Ine kulibwino ndigone pa mimba yanga ndi kudya zikondamoyo za chidulo ndi kumamwa madzi a mngalande, ndi kukhala woyera ndi wangwiro pamaso pa Mulungu, kuposa kunyengerera chifukwa cha mtundu uliwonse wa ntchito. Ndiko kulondola. Zoonadi. Khalani owona kwa Mulungu.

⁷⁶ “Samsoni, Afilisti ali pa iwe.” Branham Tabernacle, chidziko chikukwawira mkati pakati panu. Bwanji zimenezo? Kodi mwaulula chinsinsi chanu? Kodi mwaulula chinsinsi chija chimene Mulungu anakupatsani inu pamene inu munali kugudubuzika mmenemo mu utuchi zaka pang’ono zapitazo? Kodi mwakulola iko kukwawira kunja ndi kupembedza kwa chitukuko, kwamawonekedwe? Nchiyani chachitika kwa inu? Mulungu akhoza kubwera pansu ndi kuchita chozizwitsa ndi

kuyendayenda kudutsa mwa omvera ndi kuwauza anthu zinsinsi za mitima yawo, ndi chirichonse, ndi kuchiza odwala ndi osautsika, ndi kuchita zizindikiro ndi zodabwitsa, ndi kulalikira Mawu Ake molimba monga iwo angakhoze, mwa Mzimu Woyera; ndipo anthu nkumati, “Chabwino, ine ndikuganiza izo ndi zabwino. Ife timasangalala kumvetsera kwa izo kamodzi mu nthawi, ngati ife sitiri otopa kwambiri.” Ndiyo Branham Tabernacle. Afilisti ali pa iwe.

⁷⁷ Pamene, zinkakhala kuti pamene Mawu akulalikidwa, ndipo oyera akale ali ndi misonzi mu maso awo, ankawuka ku mapazi awo ndi kuyenda, akulira, mwina osanena mawu, kumangoyenda pozungulira, nthawi ziwiri kapena zitatu, ndi kukakhala pansu, odzazidwa kwambiri ndi Mzimu Woyera! Mawu ankawadyetsa iwo! “Munthu sadzakhala moyo ndi mkate wokha, koma ndi Mawu alionse amene atuluka kuchokera mkamwa ya Mulungu.” Afilisti ali pa iwe, Branham Tabernacle.

Afilisti ali pa iwe, Wachipentekoste.

⁷⁸ Zoonu, Afilisti akugwirani inu, nonse a inu, nthawi yayitali kale pamene inu munadzipanga nokha bungwe mothina kwambiri, palibe kanthu kakanakhoza kubwera mkati kupatula inu mutakhala Mpresibateria, Mbaptisti, Mmethodisti, Mkatolika, kapena chinachake. Iwe siumakhala ndi chochita ndi ena onse a iwo.

⁷⁹ Kotero, chitsitsimutso mu tsiku lathu? Ife tingakhoze kukhala nacho motani icho pamene wopereka-chitsitsimutso nthawi zonse wamangidwa ndi dziko? Mulungu sangakhoze kubwera mkati mmene dziko lirimo, inu mukhoza kungodalira pa zimenezo. Inu mukamayanjana nalo dziko, ndiye ndizo—ndizo zonse za izo. Pamene inu mulola dziko kukwawira mkati, inu mukamapita mukumakachita monga dziko, ndiye inu mwathedwa. Koma pamene inu mungadule momasula chingwe chirichonse kuchoka ku dziko, ndi kubwera kwa Mulungu, Mulungu akugwiritsani inu ntchito mpaka inu mutapita komakadziyalutsa kachiwiri.

⁸⁰ Pano pali chiyembekezo chokhacho chimene ine ndiri nacho mmawa uno, kuti nditsirizitse Uthenga wanga, ndi ichi. “Pamene Samsoni anali atamangidwa, mulu watsopano wa tsitsi unamera.”

⁸¹ Mulungu, titumizireni ife Mpingo wina isanafike kumene nthawi yotsiriza, kuti Mphamvu ya Mzimu Woyera ikhoza kubwera mwa iye, mwa ziwonetsero za Mzimu, ndipo Marko 16 akhoza kuwutsatira Mpingo. Machitidwe 2:4, Machitidwe 2:38, zonse za izo zidzatsatirana limodzi kumene ndi Mpingo. Zizindikiro ndi zodabwitsa zinawatsatira atumwi. Zizindikiro zazikulu za chiwukitsiro Chake zinawatsatira iwo. Pamene ife tiri mu ndende, zedi Mulungu akumeletsa mbewu kwinakwake, za kupha kotsiriza kwakukulu. Mulole mukhale inu, mzanga

wa Chikhristu pano mmawa uno, mulole zikhale mphamvu zanu kuti zayamba kukula. Ine ndikupemphera kuti Uthenga uwu mmawa uno, ndi kunja kupita mu dziko kumene uwu uti udzapite, ine ndikudalira kuti Uthenga uwu udzathandiza kubweretsa mavitamini ku kuchita kwanu kuti kudzameletse Mphamvu yauzimu kubwereranso mu moyo wanu kachiwiri.

Tiyeni ife tiweramitse mitu yathu ndi kupemphera.

⁸² O Ambuye Mulungu, Mlengi wa Miyamba ndi dziko lapansi, Mwini wa Moyo Wosatha, ndi Wopereka wa mphatso iliyonse yabwino ndi yauzimu, tengani mawu awa mmawa uno ndipo muwayike iwo mu mtima, ndi kuwatsirira iwo, Ambuye. Mulole anthu apempherere zinthu izi, powona kuti dziko lawunyengerera mpingo ndipo potsiriza lapeza Mphamvu zake, lapeza malo ake achinsinsi, lapeza pamene pakugona chinsinsi chake, ndipo lazimeta izo. Lawatenga anthu amene nthawiyina anafuulapo chigonjetso, nthawiyina anali nacho chigonjetso, ndipo lawameta iwo, kuti azikhala mmakwawo Lachitatu usiku kuti aziwonera purogaramu ya televizioni. Lachotsa chimwemwe kuchokera mmitima yawo, ndi kuwapatsa iwo chikondi chochuluka kwa dziko koposa chimene iwo ali nacho kwa Mulungu. Lawapatsa iwo dziko lochuluka, kwa zachidziko, chikhumbo chochuluka cha zosangalatsa zachidziko kuposa kukhala ndi kulalikira kwa Uthenga. Ngati palibe gulu lalikulu ndi zochuluka za kumangopitiriza, ndi kuphokosera ndi kumapitiriza, ndiye iwo sakuwufuna Uthenga wakale, panonso, umene umabweretsa misonzi ya chimwemwe kwa solo, umene umabweretsanso machiritso Auzimu, umene umabwezeretsa mphatso zautumwi kwa mpingo, umene umabweretsa mkati Khristu wowukitsidwa, Mesiya wa tsiku lino.

⁸³ Koma monga Israeli anamangidwa ndi—ndi mafumu awo, kuti iwo samakhoza kutsatira Mfumu yeniyeni; ndipo Mfumu yeniyeni, pamene Iye anabwera, iwo sanamuzindikire Iye. Kotero izo ziri lero O Ambuye, Mfumu ya Ulemerero yawonekera mu mawonekedwe a Mzimu Woyera, ndipo, Ambuye, iwo sakuzidziwa zimenezo. Iwo sakuzizindikira izo. Iwo ali abungwe mothina kwambiri, mwakuti iwo sakumvetsa zimenezo, chifukwa izo siziri mu bungwe lawo. Ambuye, iyi ndi ntchito ya Mdierekezi imene yachita izi kwa anthu.

⁸⁴ Mulole Samsoni wa Mulungu, mulole owona mu mtima, iwo amene akuyembekezera ndi kulira, ndi kuchondelera ndi kugwiritsabe, mulole iwo akhale ndi icho, Ambuye, mpaka mbewu yatsopano iyi itakula, mpaka apo patabwera kachiwiri chimwemwe mu Zioni, ndipo pamenepo patabwera gulu limene lingakhoze kuzindikira ndi kumvetsa, limene lingakhoze kumuwona Mesiya ndi Mphamvu yobisika imene yabisika kwa dziko, zimene iwo sakanazimvetsa izo tsopano. Perekani, Ambuye, kuti iwo awone izi. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

[Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.]

. . . Mphamvu pano,
O Ambuye, tumizani Mphamvu
Mubatize aliyense.

Anali mchipinda chapamwamba,
Anali mwa mtima umodzi,
Mzimu Woyera unatsika
Wolonjezedwa ndi Ambuye.

O Ambuye, tumizani Mphamvu,
O Ambuye, tumizani Mphamvu;
O Ambuye, tumizani Mphamvu
Mubatize aliyense.

⁸⁵ Momwe ine ndimamukondera Iye! Angotumiza Mphamvu Yake! Iwo anali mu chipinda chapamwamba, onse mwa mtima umodzi. Dziko lonse linali litakhuthuka mwa iwo. Iwo anali atadzitsanula, ndipo Mzimu Woyera unabwera.

⁸⁶ Lero iwo akuti, “Bwerani, mudzajowine mpingo, dzaikeni dzina lanu pa bukhu. Kapena gwadani pansi ndi kuti, ‘Ine ndikumuvomera Khristu ngati Mwana wa Mulungu,’ dzukani.” Mdierekezi amachita chinthu chomwecho. Ndithudi. Mdierekezi anabatizidwa pamene Yudasani anabatizidwa. Mdierekezi anapita kunja ndi kukalalikira Uthenga pamene Yudasani anapita kunja ndi kukalalikira Uthenga. Koma Mdierekezi sanalandire Mzimu Woyera. Ndi zimenezo. Apo ndi pamene pali Mphamvu yobisika, chiwukitsiro chija, imene imadziwa zotheka, kupyola mthunzi wa kukayika. Amen.

⁸⁷ Iye ali pano. Mzimu Woyera yemwe uja, Womwe uja unali pa Mesiya, ukadali pa Mpingo Wake. Iye samachoka konse. “Ine ndidzakhala ndi inu nthawizonse, ngakhale mkati mwa inu, mpaka kumapeto a dziko. Ine ndidzakhala kumeneko. Ntchito zimene Ine ndikuzichita, inu mudzazichitanso. Zoposa izi inu mudzazichita, pakuti ine ndikupita kwa Atate Anga.”

⁸⁸ Koma dziko limanyengerera pa izo, “O, amenewo ndi masiku akale!” Basi chimene Mdierekezi akufuna inu kuti muchite. Iwo akufuna inu mukongoletse. Mulungu akufuna inu mubatizidwe. Mulungu akufuna inu. . . Inu mukuti, “O, ine sindikukhulupirira zonse izo zimene iwo akumapitiriza.” Pitirizani ndipo mukakhale, pitirirani ndi kumakhala mu tchimo lanu, zikhalani mu tchimo lanu. Koma mpaka inu mutavunda, mpaka inu mutavunda kwa malingaliro anu omwe, mpaka inu mutavunda kwa mafashoni anu omwe, ndi kusinthidwa kachiwiri ndi kubadwa kachiwiri, ndipo Moyo watsopano uwo udzakhala palimodzi wosiyana kwa uwo umene unapita pansi.

⁸⁹ Njere ya chimanga imapita pansi yachikasu, iyo imatulukira yobiriwira. Imapita pansi yolimba, yokutidwa mkati, iyo imatuluka yofewa ndipo ikukupizidwa ndi mphepo. O,

ulemerero! Aleluya! Pamene mphepo zinayamba kuwomba, njere siyingakhoze kuchita kanthu koma kudzisuntha yokha, kusamuka, koma aang'ono—masamba aang'ono amafewa ndi kusangalala, amakula ndiye, kudzilimbitsa okha. Iwo sangakhoze kukhala masamba mpaka chimanga chitafa ndi kuvunda. Osati kokha kufa; koma kuvunda. Sangakhoze kubwerera panonso, koma moyo umabwera kuchokera mwa iwo.

⁹⁰ Monga ine ndinanena kanthawi kapitako, kubadwa ndi chinthu chonyansa, chauve, zoyipa, chonyansitsitsa cha zanyansi, koma ndi pamene moyo wagona. Pamene iwe udzizindikira wekha wauve, kuzindikira Methodist yako, Baptisti ndi zikhulupiriro za Chipentekoste ngati nyansi, ndi kufera apo pa guwa, ndiye Moyo watsopano umabwera mkati. Mzimu Woyera umakupangitsani inu mkatimo pamwamba pa zimenezo; inu mumamuwona Mulungu.

⁹¹ Ife tidzamuwona Iye tsiku lina laulemerero. Tsiku lina kupitirira kofika kwa thupi la chivundi, ife tidzamuwona Iye. Inu mukukhulupirira zimenezo? Tsiku lina kupitirira kofika kwa thupi la chivundi, uko likundiyebekezera ine mawa lokoma.

⁹² Ine ndinali kuyima pamwamba kuno pa ngodya usiku watha, ndipo ndimaganiza kuti ine ndinamuwona Rabbi Lawson wamng'ono. Pamene iye anakonda kukhala kumusi kuno, ndi kufikira pozungulira ndi ndodo yake yakale ndi kundikoka ine ndi khosi lake, pa khosi langa ndi ndodo yake, pamwamba pano ku guwa, ndi kumayimba nyimbo ija, “Uko akundiyebekezera ine . . .” [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.]

⁹³ Chinachake chinachitika! Ichu chinachotsera dziko kunja. Ine ndinayamba kuwona zinthu mosiyana. Ine ndadandaula mochuluka kwambiri za momwe anthu Achimereka awa akuchitira, mowirikiza, chaka ndi chaka, kuwawona akazi ndi amuna momwe iwo akudzinyozetsera okha ndi kumatuluka mu tchino, mpaka ine ndinali nako kusweka, kawiri kapena katatu, kudandaula pa izo. Dzulo, ine ndinanena kwa Mulungu, “Ine sindidzadandaula kenanso. Mawu anu anati izo zidzakhala chomwecho. Koma ine ndidzayima pakati ndi kuyitana motsutsa izo, ndi zonse zimene ziri mwa ine.”

⁹⁴ Tsiku lina, nditayima uko ku Mtchini wa a Green, mphanga yanga, kutali mmbuyo mu nkhalango, ndinali ndikupemphera tsiku lonse. Ndipo pafupi firii koloko, dzuwa linali likulowa, ndipo ine ndinali kuimirira kumeneko ndikuyang'ana chopingasa, ndinatuluka mu mphangamo, kukhala pamwamba pa thanthwe lalikulu. Ndipo ine ndinali kuima pamenepo, ine ndinayang'ana cha Kummawa, ndikuwayamika Ambuye. Ndipo ine ndimakhoza kuliwona dzuwa likusunthira pansu kuseri kwa mitengo mmwamba pamwamba pa phiri, pamene ine ndimayang'ana modutsa chigwa kupita ku yina, ndipo pali

maluwa ochuluka, mwabata basi monga iko kukanakhoza kukhalira. Ndipo ine ndinati, “Ambuye, tsiku lina Inu munamubisa Mose mu mphanga ya thanthwe, ndipo Inu munadutsa pafupi ndi iye, chifukwa iye anali akudandaula. Koma Inu munadutsa pafupi, iye anati iwo ‘unawoneka ngati nsana wa munthu.” Ine ndinati, “Ndibiseni inu mu thanthwe, Ambuye.” Pafupi nthawi imeneyo, cha ku mbali imodzi ya ine, uko kunabwera Mphepo yaing’ono ikusuntha kumka chodutsa tchire. Iyo inasuntha motsatira kumene, inabwera mmunsi cha ku mbali yanga, Mphepo yapang’ono ikusunthira mmunsi, inapita pansu kupyola mnkhalangomo. Ine ndinayima pamenepe.

Tsiku lina, Mulungu yekha akudziwa kuti ndi liti,

Magudumu a moyo wachivundi adzayima njo,
Ndiye ndidzapita kukakhala pa phiri la Zioni.

Tsiku lina kupitirira kofika thupi la chivundi,
Tsiku lina, Mulungu yekha akudziwa kuti ndi liti,

(Chiyani chiti chidzachitike? Iye adzatseka,
magudumu onse aang’ono awa
kugudubuzika.)

Magudumu a moyo wachivundi onse adzayima
njo,
Ndiye tidzapita kukakhala pa phiri la Zioni.

Tsikira pansu, galeta lokoma,
Tsikira kudzanditengera Kwathu;
Tsikira pansu, galeta lokoma,
Kudzanditengera Kwathu.

Ngati mukafike uko ine ndisanatero,
Kudzanditengera Kwathu;
Mukamuuze M’bale Bosworth, ndi onse
abwenzi anga, nawonso,
Kudzanditengera Kwathu.

Tsopano tsikira pansu... (ilo lidzafika
pansu tsiku lina ndi kundinyamulira ine
mmwamba.) ...gale-...

(Mtengo uliwonse udzakhala ukuyaka;
Angelo a Mulungu, galeta la moto)...
kudzanditengera Kwathu;

Tsikira pansu, galeta lokoma,
Kudzanditengera Kwathu.

⁹⁵ Limodzi la masiku amenewa, limodzi la masiku amenewa mu zigawo za mmusi za maora anga a imfa, ine ndikumuyembekezera Iye kubwera. Ndiko kulondola.

Ine ndinayang'ana cha ku Yorodani kodi
 ndinaonaji
 Kudzanditengera Kwathu; (monga Eliya
 wakale akuyang'ana patsidya pa Yordani)
 Gulu la Angelo owala likubwera kwa ine,
 Anali kudzanditengera Kwathu.

Tsikira pansi, fika pansi pafupi, galeta lokoma,
 Kudzanditengera Kwathu;
 Tsikira pansi, galeta lokoma,
 Kudzanditengera Kwathu.

⁹⁶ Ambuye Yesu, Dalaivala wodalitsika wa galeta ili, Woyendetsa wa ngalawa yakale ya ku Zioni, bwato la Moyo, akusunthira pansi kudutsa mu nyumba ino, akuyankhula, Kukhalapo Kwake kuli pano. Mzimu Woyera womwewo umene unamuwukitsa Iye kuchokera ku manda uli pano.

⁹⁷ Pokhala kuti iwo sanapereke ayi makadi a pemphero, kodi alipo aliyense pano yemwe wabwera kuchokera kunja kwa tawoni, yemwe ine sindikumudziwa, yemwe ali pano kuti apemphereredwe? Kwezani manja anu, omwe ine sindikuwadziwa. Kwezani manja anu, ine sindikukudziwani. Inu, inu apo. Ine ndikukhulupirira munthu wamng'ono ali ndi masharubu kumbuyo ukoyo, winawake anakweza dzanja lake kumbuyo cha kumeneko. Eya, inu, kodi inu munakweza dzanja lanu? Chabwino. Kumbuyo uko, inu, bwana. Chabwino. Inu nonse ndinu alendo kwa ine? Ambuye Yesu ameneyo, M'busa yemweyo wa nkhosa pano, kodi inu mukukhulupirira malonjezo Ake ali owona? Iye amaudzoza mpingo Wake, ndipo "Ntchito zimene Ine ndizichita, mudzazichita, inunso. Ngakhale zoposa izi inu mudzachita, pakuti Ine ndikupita kwa Atate Anga. Zoposa izi!" Inu mukukhulupirira zimenezo?

⁹⁸ Kodi inu munakweza dzanja lanu kuti inu simumandidziwa ine? Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kundiuza ine chimene chiri mu mtima wanu, akhoza kuyankhula kwa ine monga ngati Iye anachitira mkazi atakhudza chovala Chake? Kodi inu mukukhulupirira kuti Iye ali Wansembe Wamkulu yemwe angakhoze kukhudzidwa ndi kumverera kwa zowawa zathu? Ngati Mulungu ati aulule kwa ine momwe muliri, kodi inu mundikhulupirira ine kuti ndine Mneneri wake, kukhulupirira kuti Kukhalapo Kwake kuli pano ndipo ndi chifukwa chake Iye akuloleza izo? Inu mukupempherera akazi anu. Iwo ali ndi ntchafu yosweka, ntchafu yosemphana. Ndiko kulondola. Ngati ndiko kulondola, ukani. Chabwino, pitani mukamupeze iye, wabwino. Amen.

⁹⁹ Nanga bwanji za inu kumbuyo uko, munthu wamng'ono yemwe unakweza mmwamba, yemwe anali ndi masharubu? Iwe ukukhulupirira ndi mtima wako wonse? Kodi iwe ukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kundiuza ine mavuto

ako? Kodi iwe ukukhulupirira kuti mwana wako achira? Iwe ukutero? Uli ndi mwana, iye ali ndi khunyu la ubongo. Ndiko kulondola. Inu simuli ayi...Ndiye wochokera ku Kentucky. Ngati ndiko kulondola, kwezani manja anu. Ine sindikukudziwani, inu, ndichoncho ine? Ngati ine ndikukudziwani...Kwezani manja anu monga *chonchi*, ife sitikudziwana wina ndi mzake. Ndiko kulondola. Tikudalira kwa Mulungu. Kodi inu mukukhulupirira? Pamene inu mukukhulupirira, kampezeni mnyamata wanu momwe inu mukukhulupirira. Ndangokuyikirani inu pa mtima wanu.

¹⁰⁰ Anali ndani apa amene anakweza mmwamba manja awo, omwe ine sindinati—sindinati...Kodi munali inu? Chabwino, bambo, kodi inu mukundikhulupirira ine kuti ndine mneneri wa Mulungu? [Munthuyo akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Inu mukutero, ndi mtima wanu wonse? Inu simukusowa kuwuka, ingoyimani apo pomwe. Chabwino, bwana, lomwe liri vuto lanu, inu muli ndi matenda a shuga. [“Ndiko kulondola.”] Ndipo ilo likuvutitsa phazi lanu. [“Eya.”] Ndinu wochokera ku Ohio. [“Eya.”] Dzina lanu ndinu Bambo Miller. [“Ndiko kulondola.”] Bwererani kwanu ndi kukakhala bwino. Chabwino, khulupirirani ndi mtima wanu wonse. Chabwino.

Inu mukukhulupirira ndi...Khulupirirani izo. Ngati inu mungakhoze kukhulupirira!

¹⁰¹ Dona wakhala apa, kodi inu munakweza dzanja lanu? Dona wamkulu, wavala magalasi, inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse? Kodi inu mukukhulupirira ndi... Inu mukundikhulupirira ine kuti ndine wantchito wa Mulungu? Inu mukutero? Chabwino, ngati Mulungu angakhoze kundiiza ine lomwe liri vuto lanu, kodi inu mukhulupirira? Vuto la mtima. Chabwino, kwezani dzanja lanu mmwamba ngati ndiko kulondola. Chabwino.

¹⁰² Dona pano pafupi ndi inu, munakweza mmwamba. Mtima; koma ndiwo kwenikweni maso anu. Ine ndikumudziwa iye. Chabwino, ngati inu mungakhoze kungokhulupirira!

¹⁰³ Kumbuyo uko, munthu wotsatirayo kumbuyo uko ali ndi vuto la mtima, nayenso, ndi matenda a khungu. Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu angakupangeni inu kukhala bwino? Inu mukutero, bwana?

¹⁰⁴ Kuli mwamuna kumbuyoko penapake, anakwezera mmwamba manja ake yemwe sanati...Bambo Schubert. Chabwino, bwana. Chabwino, kodi inu mukukhulupirira? Ndi za maso anu, nawonso, sichoncho? Inu mukuwapempherera amayi anu akhala kunja uko, nawonso. Ngati ndiko kulondola, kwezani mmwamba dzanja lanu. Ndife alendo. Kulondola uko? Gwirani dzanja lanu, gwiranani dzanja lanu kwa wina ndi mzake. Chabwino, ndiko kulondola. Ngati inu mungakhoze kukhulupirira, inu mukhoza kulandira!

105 Yesu Khristu wowuka ali mchipinda. Iye ali Mmodzi yemweyo. Kodi Izo zikuchita chiyani kwa inu? Kodi mwalilola dziko kuyamwa mphamvu zonse kuchokera mwa inu? Ulemerero! Ine ndikufuna kubadwa kwatsopano! Ine ndikufuna Moyo watsopano! Ine sindikusamala kaya Iwo ubwera pa malo otani, ngati ine ndiyenera kuti ndikhale woyera wodzigudubuza, chirichonse. Ine sindikusamala malo otani Iko kutabwereco, ine ndikufuna Mzimu Woyera weniweni monga uli pa ine tsopano. Ine ndikufuna kuwusunga Iwo! Ine kuli bwino ndikhale nawo Iwo kuposa zinthu zonse za mdziko. Ameni! Kodi inu mukukhulupirira? Kodi inu mukukhulupirira kuti Iye ali pano?

106 Ikani manja anu pa wina ndi mzake, ndiye. Ndiuzeni ine chinthu china chowonjezera chimene Iye angakhoze kuchita. Palibe. Khalani ndi chikhulupiriro tsopano. Khulupirirani kuti izo zatha.

107 Ambuye Mulungu, Mlengi wa Miyamba ndi dziko lapansi, Mwini wa Moyo Wamuyaya, ndi Wopereka wa mphatso zabwino zonse, Mzimu Wanu uli pano ukudzoza chotero, Ambuye, zikuwoneka ngati nyumbayi ikupuma, ikusunthira mmbuyo ndi mtsogolo. Chifukwa chiyani anthu sangamvetse izo, Ambuye? Kodi iwo—iwo ayanjana nalo dziko mochuluka chotero, ndipo azizira chotero ndi mwamawonekedwe ndi okhuthara, mpaka iwo sangakhoze kukudziwani Inu kenanso? Ambuye Mulungu, mulole Mphamvu iyi ikanthe aliyense, ndi munthu aliyense wodwala achizidwe, wochimwa aliyense apulumutsidwe, ndipo Mulungu tengani ulemerero. Kupyolera mwa Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu, ine ndikupempha izi. Ameni.

108 Kodi inu mukukhulupirira izo? Kwezani mmwamba manja anu. Kodi inu mukulandira machiritso anu? Mulungu akudalitseni inu. Tsopano pitani ndipo mukawapeze iwo basi momwe inu mukukhulupirira, izo zikakhala mwanjira imeneyo. Ine ndikuwona masomphenya akuphulikira pa ena. Ndiko kulondola. Ine ndiyenera kubwerera usikuuno.

109 Ngati inu simukukhulupirira tsopano, inu simudzakhulupirira konse. Ndiko kulondola. Yesu anachita izo nthawi imodzi, ndipo iwo anati, “Inu muli. . . Ife tikudziwa pamene Mesiya abwera, Iye adzatiuza ife izi.” Iye anati, “Ine ndikudziwa Mesiya adzachita zimenezo. Koma Ndinu Yani?”

Iye anati, “Ine ndine Iye.”

110 Ndiye iye anathamanga kupita ku mzinda ndipo anakati, “Bwerani, mudzamuwone Munthu Amene wadziwa chimene ine ndinali ndi zimene ndachita. Kodi sali uyu Mesiya?”


111 Iye anati, “Zinthu izi zidzapangidwa kachiwiri mu masiku otsiriza. Mpingo udzakhala ukulalikira Choonadi, Iwo udzakhala ukuyima pa Mawu. Iwo udzakhala ukuchita Malamulo onse a Mulungu. Iwo sudzayanjana nalo dziko.

Ndipo kupyolera pamenepo Ine ndidzasuntha ndi kuchita zinthu zomwezo.”

¹¹² Koma Iye anati, “Iwo adzakhala ammutu, amaganizo apamwamba, okonda zosangalatsa koposa kukonda Mulungu, okuswa pangano, onamizira amzawo, okhala nawo mawonekedwe aumulungu,” achipembedzo kwambiri, akupita ku mipingo. “Okhala nawo mawonekedwe aumulungu, koma kumakana Mphamvu yakeyo. Kwa oterowo muchokeko!”

¹¹³ Inu anthu, kulikonse kumene inu munali mu mpingo, amene Iye wakuyitanani pakali pano, masomphenya achoka kwa ine. Ngati—ngati izo zinali zoonadi, zimene ine ndinanena, ndipo ine pokhala kuti sindimadziwa izo kwa inu, kwezani manja anu, yense yemwe anali. Mu mpingo wonse, aliyense—munthu aliyense. Chabwino. Mwaona? Sindikuwadziwa iwo, sindinawawonapo iwo; koma Mzimu Woyera uli pano ndipo Iye akuwadziwa iwo. Kodi inu simukukhoza kuwona kuti si ine?

¹¹⁴ Mvetserani! Ngati Iye angati andidalire ine ndi zimenezo, Iye andidalira ine ndi Choonadi cha Mawu, chifukwa Choonadi chikhoza kubwera kokha mwa Mawu. “Lapani, aliyense, ndi kubatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu, kwa kukhululukiridwa kwa machimo, ndipo inu mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera, pakuti lonjezo liri kwa inu ndi kwa ana anu, iwo amene ali kutali, ngakhale ochuluka amene Ambuye Mulungu wathu adzawaitana.” Inu mukukhulupirira izo? Payenera kukhala utumiki wa ubatizo mu mphindi chabe.

¹¹⁵ Tiyeni tiweramitse mitu yathu. Ine ndiwapempha abusa kuti apemphere pamene iwo akukonzekera ubatizo. Ine ndikuganiza pali utumiki wa ubatizo umene ukubwera. Chabwino. 

Mpingo Ndi Chikhalidwe Chake
(*The Church And Its Condition*)
Ogasiti 5, 1956, Lamlungu Mmawa

Khwalala Ndiro Chipata
(*Strait Is The Gate*)
Marichi 1, 1959, Lamlungu Mmawa

Mpingo Wonyengedwa Ndi Dziko
(*A Deceived Church, By The World*)
Juni 28, 1959, Lamlungu Mmawa

Mauthenga awa a M'bale William Marrion Branham, anaperekedwa pachiyambi mu Chingerezi ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., atengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito ndipo anasindikizidwa mu Chingelezi. Maulaliki awa anamasuliridwa mu Chichewa ndi kudindidwa mu 1997 ndi:

CHICHEWA

©1997 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org